

MULUNGU NDIYE *mphamvu* YATHU

Tsiku la Kupemphera ndi Kusala kudya pa Dziko lonse lapansi - 12 January 2022

Kutamanda

Mulungu ndiye **mphamvu** yathu: chifuniro, chikhalidwe, malingaliro, kapena cholinga chake n'chosasinthika pa ife Chauta ndiye mfumu. Wavala ulemerero, wavala **mphamvu** ngati lamba. Iye adakhazikitsadziko lapansi, silidzagwedezeka konse. **Salimo 93:1**

Ulemerero ndi ufumuzili pamaso pake, **mphamvu** ndi chimwemwe zili m'Nyumba mwake. **1 Mbiri 16:27**

Kungani **mphamvu** zanu, Inu Mulungu, onetsani **mphamvu** zanu, Inu Mulungu, amene mumatichitira zamphamvu. **Salimo 68:28**

Pa tsiku limene ndidakuitanani, Inu mudandiyankha, mumandilimbisa mtima ndi **mphamvu** zanu. **Salimo 138:3**

Kulapa

Motero Iye **adzalimbisa mitima** yanu kuti idzakhale yangwiro ndi yoyera pamaso pa Mulungu Atate athu, pamene Ambuye Yesu adzabwerenso Pamodzi ndi oyera ake onse. **1 Atesalonika 3:13**

Kuthokoza

Koma ndidzayimba nyimbo zotamanda mphamvu zanu, m'mawa ndidzayimba mokweza nyimbo zoyamika chikondi chanu chosasinthika; pakuti Inu mwakhala ngati linga langa ndi malo othawiramo pa nthawi ya mavuto anga. **Salimo 59:16**

Kupempherera ena

Ana athu

Uzikonda Chauta, Mulungu wako, ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi **mphamvu** zako zonse, ndi nzeru zako zonse, ndiponso mnzako monga momwe umadzikondera iwe wemwe. **Luka 10:27**

Aphunzitsi, ophunzira, ogwira ntchito pasukulu okhulupirira

Muzidalira Chauta ndi **mphamvu** zake; muziyesetsa kukhala pamaso pake kosalekeza. **Salimo 105:4**

Aphunzitsi, ophunzira, ogwira ntchito pasukulu osakhulupirira

Ngati ubvomereza ndi pakamwa pako kuti Yesu ndi Ambuye, ndipo ukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu adamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka. **Aroma 10:9**

Nkhawa za sukulu

Tamandani Chauta, inu anthu a mitundu yonse, bvomerezani kuti ulemerero ndi **mphamvu**, zones n'za Chauta.

Nkhawa za Amayi aPemphero

Inu mphamvu zanga, ndidzakuyimbirani nyimbo zokuyamikani, pakuti Inu Mulungu ndinu linga langa, ndinu Mulungu wondiwonetsa chikondi chosasinthika. **Salimo 59:17**

Ndingathe kuchita zonse chifukwa Khristu amandipatsa mphamvu. **Afilipi 4:13**

Kudalitsa

Mulungu Atate athu adatikonda, ndipo mwa Kukoma mtima kwake adatipatsa kulimba mtima kosatha ndi chiyembekezo chokoma. Iye pamodzi ndi Yesu Khristu Ambuye athu athuzitse mitima yanu ndi kukupatsani **mphamvu** za kuchita nci kulamkhula zabwino zilizonse. ... Ambuye aongolere maganizo anu kuti muziyena m'chikondi cha Mulungu, ndi kutsata khama la Khristu. **2 Atesalonika 2:16-17, 3:5**